NYA_TTB_1070_SCRIPT

2 Petro : 3:5-10

Mutu : Mulungu ali ndi chikonzero cha padziko lapansi

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolera ndi mau apaAhebri 12:11, pamene akuti, “Chilango chiri chonse pakuchitika, sichimveka chokondweretsa, komatu chowawa; koma chitatha, chipereka chipatso cha mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa nacho, ndicho cha chilungamo.”

Mupologalamu yatha tinali ku kambirana pa 2 Petro 3:1-7, 13, pomwe timasanthula zakubwera kwa Kristu kachiwiri, kuti kudzakanidwa ndi aphunzitsi onyenga. Ndipo lero pa 2 Petro 3:5-10, tikambirana za chikonzero cha Mulungu chapa dziko lapansi.

5. Pakuti ichi aiwala dala kuti miyambainakhala kale lomwe, ndi dziko lidaungika ndi madzi ndi mwa madzi, pa mau a Mulungu;
6. Mwa izi dziko lapansi la masiku aja, pomizika ndi madzi, lidaonongeka;

Mtumwi Petro afuna kutifulumiza ndi kutitakasa kuti tikhale tcheru ndi wolimba kuzimene Mulungu adatibvumbulitsiraife kudzera mwa aneneri ndi Atumwi kuti kudzabwera anthu amene adzatsutsa za chilango chobwera m'masiku otsiriza. Komanso anthu onyozawa, adzatsutsanso za njira ya Mulungu yopulumutsira anthu ochimwa kudzera mwa Yesu Kristu m'masiku otsiriza.

Awa, ndiwo anthu amene safuna kudziwa za chilango cha m'masiku otsiriza.Kutanthauza kuti anthu amenewa amaonetsa kusadziwa kwawo mwadaladala.Kunena kuti kusadziwa kwawo ndikochita kufuna kapena kukonza kuti asadziwe.Ili, ndilo ganizo lomwe likutsutsana ndi mau a Petro pa 2 Petro 3:8, omwe akuti, "Koma ichi chimodzi musaiwale okondedwa inu, kuti tsiku limodzi likhala kwa Ambuye ngati zaka chikwi, ndi zaka chikwi ngati tsiku limodzi."Ndiye anthu otsutsawa ndiwo amene amatseka maso awo mwadalakuzolembedwa m'mau a Mulungu za chilengedwe ndi chionongeko cha dziko ndi madzi. Ndiye Petro akunena kuti, iwo amene ali ndi ganizo lakuti zinthu zonse zidzapitilira kukhala monga momwe ziri osasintha konse, ndiwo anthu amene akhala

osadziwa kuti zinthu sizinali chomwechokalelo. Kunena kuti kale m'mbuyomo kunadza chionongeko cha dziko chifukwa cha chigumula cha madzi m'masiku a Nowa.Ndiye nkhani ikuti anthu onyozawa anasankha kusaona zomwe zinachitika kalelo.Tikunena kuti ngakhale anadziwa kapena amayenera kudziwa, koma iwowa anasankha kukhala wosadziwa, nalubza dala nakhala ngati kuti sanamvepo kanthu kena kalikonse zokhudza chionongeko cha dziko.Kutsimikiza kuti ngati iwowa anamvapo ndiye kuti sanafunakusunga chimenechi. Mwanjira ina Petro akunena kuti ichi, ndichinthu chomwe chinabisidwa kwa anthu amene amakana ziphunzitso za m'Baibulo. Taonani kuti anthu onyozawa amanena kuti malamulo a chilengedwe cha dziko ndi omwewo, sanasinthe konse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti ndichinthu chobvuta kwambiri kuyesa kupanga munthu kuti akhulupirire chinthu chomwe iye sakufuna kuona kuti ndichoona.Munthu wotereyu amakhala wosadziwa nthawi zambiri chifukwa amakhala wofuna kukhala wosadziwa.Ndipo munthu ameneyu sadziwa kuti sadziwa chifukwa salabadira kuti adziwe. Koma munthu

wochimwa sayenera kuganiza kuti kusadziwa kumeneku, kudzabvomerezeka kapena kudzalandiridwa kukhala chifukwa chakuti asalandire chilango chifukwa cha tchimo lake ayi. Tamvani Paulo pa 1 Akorinto 2:8, akutsindika kunena kuti, “Imene saidziwa m’modzi wa akulu a nthawi ya pansi pano: pakuti akadadziwasakadapachika Mbuye wa ulemerero.” Paulo akunena kuti anthu aja anapachika Ambuye Yesu sanadziwa kuti Kristu anali yani?Chifukwa akanadziwa, sakadampachika Ambuye waulemerero.Koma nkhani ikuti ngakhale anthu awa samadziwa, sizikutanthauza kuti ndiwosachimwa ayi, chifukwa kusadziwako ndilo tchimo lomwe anasankha kuti asadziwe.Pachifukwa chimenechi tikunenetsa kuti palibe tchimo lomwe lingapulumutse kapena kulanditsa tchimo linzake.Momwemo Mtumwi Petro akunena kuti anthu onyozawaakadadziwa za chilango choopsa chomwe chinagwera anthu ochimwa padziko lonse lapansi nthawi imeneyo, sakadanyozera chenjezo lomwe iye anapereka.Koma anthu amenewa anali wosadziwa chifukwa anasankha kuti asadziwe kukhala wosadziwa chomwe Mulungu anachita kale.

Tsono Petro akufusa kuti, kodi chionongeko chomwe chinachitika ndi dziko lakalelo, sichinali kusintha kwa dziko? Ndiye akuti kusintha uku kunali koopsa ndithu, chifukwa kunachitika ndi mau aulamuliro a Mulungu ndi lonjezo lomwe adanena pa Genesis 6:7, pamene adati, “Ndipo anati Yehova, ndidzafafaniza anthu amene ndawalenga pa dziko lapansi; anthu ndi nyama, ndi zokwawa, ndi mbalame za m’mlengalenga: pakuti ndimva chisoni chifukwa ndapanga izo.” Uku, ndiko kusintha kumene anthu onyozerawasadakuone.

Ndiye tsopano tiona zomwe Mtumwi Petro akunena kuti kukudzanso kusintha kwina komwe kukubwera ndi chionongeko. Tamvani;

7. Koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mau omwewo zaikikakumoto, zosungika kufikira tsiku la chiweruzo ndi chionongeko cha anthu osapembedza.

Mauwa akunena kuti dziko lino likusungidwira moto womwe ulimkudza.Nkhani ikuti Mulungu sadzaononganso dziko lino ndi madzi, koma ndi moto. Tsono ngakhale timamva ndi kuwerenga za chionongeko cha anthu ndi madzi ndipo kuti ifetimakhudzidwa,

koma tidzakhudzidwa kwambiri ndi chilango chamoto chomwe chikudza ngakhale sitingadziwe tsiku ndi nthawi yake. Ndiye tikunena kuti pamene tikumva za chilango za madzi m'nthawi ya Nowa, tipeza kuti iye ndi banja lake ndilomwe linapulumuka chifukwa linalowam'chingalawa. Koma pamene tiganizira za chilango chomwe chikudza m'nthawi yathu, chidzakhala choopsa kwambiri chifukwa sipadzakhala munthu m'modzi, kaya banja ngakhalenso mtundu wa anthu umene sudzakhudzidwa ndi chilangochi ayi. Ndiponso sipadzapezekachombochopulumukiramo kapena njira ina iliyonse yothawira ayi. Taonani kuti chilango cha chigumula cha madzi chinadza pang'ono pang'onokwa masiku makumi anayi usiku ndi usana, kotero kuti mwanjira imeneyi, anthu anachenjezedwamokwanira. Pamene chilango chomwe chikudza sichidzakhala chotere, koma chanthawi imodzi monga akunena Mtumwi pa 2 Petro 2:1, pamene akuti, "Koma padakhalanso pakati pa anthuwa aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatukoyotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okhachitayikochakudza msanga." Ndiye tikunenetsa kuti panthawi ya chionongeko cha madzi, analipo

anthu ena amene sanakhudzidwe ndi chionongekocho, koma chionongeko chomwe chikudzachi, chidzakhala cha dziko lonse, kotero kuti sipadzakhalanso malo ena, amene sadzaonongeka. Tikunena kuti sipadzakhala ngakhale Kachisi kapena church komwe anthu ena akhoza kuthawirako ayi. Uku, ndiko kusiyana komwe kulipo pakati pa chionongeko cha madzi ndi chionongeko chamoto chomwe chilimkudza. Ndiye pachifukwa chimenechi, tikunena kuti anthu amene amanyozerazakudzakwa Ambuye ndi chilango chimenechi, ayenera kulingalira mozama. Kutsimikiza kuti chilango ichi, chikubwera ndithu popeza mau a Mulungu ndiwo amene amatsimikiza chimenechi, kotero kuti ife tiyenera kudalira mau amenewa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti dziko loyamba linaonongeka ndi chigumula cha madzi, ndipo dziko lino likusungidwira chionongeko cha moto momwe oipa onse sadzapulumuka. Ndiye pali chenjezo lakuti inu simuyenera kukhala pakati pa anthu onyozera za tsiku la chilango chomwe chikudzachi. Munthu ayenera kutchera khutu ndi kumvetsa za chilangochi popeza tsiku limeneli likudza mosasintha konse ndiye

inu muyenera kudzapezekamwaKristu, momwe mudzapeza mpumulo ndi chipulumutso pamene kwa oipa, idzakhala nthawi yowawa momwe mkwiyo wa Mulungu udzaonekera.

8. Koma ichi chimodzi musaiwale okondedwa inu, kuti tsiku limodzi likhalakwa Ambuye ngati zaka chikwi, ndi zaka chikwi ngati tsiku limodzi.

Pano Mtumwi Petro akuchenjeza kuti wokhulupirira sayenera kukhala ngati anthu onyoza aja pankhani yakuchedwetsa kukwaniritsa lonjezo lake. Mtumwi Petro akukumana ndi mtsutsowakubwerakwa Ambuye Yesu Kristu chifukwa chakuti nthawi yaitari yapitapo ndipo zinthu zakhala zili monga momwe zinali. Ndiye Petro akupereka yankho lakuti munthu ayenera kuzindikira kuti nthawi kwa munthu ikhoza kuoneka kuti ndi yaitari, koma pamene ili nthawi yochepa kwambiri kwa Mulungu.

Kunena kuti m'nthawi ya Mulungu yomwe ndi yosatha, muli nthawi yochuluka kotero kuti Mulungu akhoza kutsiriza ntchito yonse yomwe inakonzedwa kuti igwirike. Ntchito imeneyi, ikhoza kugwirikam'tsiku limodzi kapena m'zaka chikwi, popeza kwa Iye kulibe kusiyana. Munthu ndiye amene ali ndi nthawi yochepa kuti

akhale ndi moyo m'dziko lapansi, ndipo ngati sangakwaniritse kuchita zolinga zake m'nthawi imeneyi, ndiye kuti sadzakwaniritsanso. Izi, ndizomwe zisiyana ndi Mulungu popeza Iye amakhala nthawi yonse, kotero kuti sibwino kuganiza kuti akuchedwa popeza ntchitoyosikuchitika ayi. Kwa Mulungu, amene amakhala nthawi yonse, ndikosabvutakutsiriza ntchito panthawi ilimkudza m'tsogolo kapena pompano. Kutanthauza kuti kukamkomerakuigwirantchitoyom'tsiku limodzi, akhoza kuchita ndithu popanda chobvuta china chilichonse, komanso akasankha kugwira ntchitoyo m'zaka chikwi, ali ndi mphamvu yonse yogwirantchitoyo. Kutsimikiza kuti munthu wochimwa sayenera kunena kuti iye akhoza kuthawa chilango chifukwa chakuti chilango chikuchedwa ayi.Komanso chifukwa chotalika nthawi, anthu wolungama amene anali pamtima pa Petro, samayenera kukaika kuti lonjezo la Mulungu silidzakwanitsidwa.Tsono chifukwa cha chikondi chomwe chikumukakamizaakuwatchula akristu amenewa kuti ndi wokondedwa ake.Ndipo akupereka upangiri wakuti, wokhulupirirawa ayenera kuika mumtima mwawo chinthu chimodzi, chomwe chingadzetse mtendere ndi kusunga chikhulupiriro ndi chiyembekezo chawo pakubweransokwa Kristu.

Ili, ndilo ganizo lomwe Mose adanena pa Masalmo 90:4, pamene adati, “Pakuti pamaso panu zaka zikwi zikhala ngati dzulo, litapita, ndi monga ulonda wa usiku.” Kutanthauza kuti ngakhale zaka makumi atatu kapena anayi zinali zitapita kale chilonjerezereni za kudza kwa Kristu, ndipo ngakhale patapita zaka chikwi kapena zikwi ziwiri, ichi sichingakhalecholetsa kukwaniritsa lonjezo la Mulungu. Kunena kuti ngakhale zaka izi, ndi zochulukakwa munthu, koma sizochuluka kuti mkulepheretsa lonjezo kwa Mulungu chifukwa kwa Iye ziri ngati tsiku limodzi. Kapena kunena kuti tsiku limodzi silisiyana ndi zaka chikwi chifukwa ndiye Mulungu wanthawiyosayamba kotero kuti zinthu zonse zakale, zatsopano ndi zomwe zidzachitika m’tsogolo, ziri pamaso pake kotero kuti kuchedwa ndi zaka chikwi, kwa Iye sizingapangitse kulepheretsa chikonzero chake ayi. Kutsimikiza kuti choona ichi, ndichomwe chingadzetse mtendere kwa inu ndi ine kotero kuti safuna kuti chinsinsi ichi, chikhala chobisikabe kwa ife.

9. Ambuye sazengerezanalolonjezano, monga ena achiyesachizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afikekukulapa.

Tiyeni pano tiyambe ndi mau akuti Mulungu ndiye wopirira; woleza mtima ndipo sapupuluma pochita zinthu ayi.Iye, sakhala ndi nkhawa chifukwa chanthawi popeza nthawi yonse ya m'tsogolo ndi yake.Kutsimikiza kuti chiweruzo chotsiriza, chionongeko chadziko lapansi ndi Kumwamba chikudza ndithu. Koma pakali pano kulikonse Mulungu akupereka mwayi wakuti munthu aliyense afike kwa Iye nalapatchimo lake. Ichi, ndichifukwa chake inu ndi ine, tiyenera kukangalikakufalitsa Uthenga Wabwino popeza ndichinthu chokhachi, chomwe chingasinthe moyo wamunthu.Kutanthauza kuti kudzera mwa mphamvu ya mau a Mulungu,yakutsutsa zolakwa zathu, munthu amabadwansokwatsopano. Ichi, ndicho chimene 1 Petro 1:23, adanena kuti, "Inu amene mudabadwanso, osati ndi mbeu yofeka, komatu yosaola, mwa mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa."

Ndiye nkhani ikuti Mulungu sali wokonzeka kuona kuti wina ataike, koma kuti afikekukulapa machimo ake.Kutsindika kuti sichifuniro cha Mulungu kuti inu mukaonongeke ayi.Tere chifukwa chimodzi chomwe inu muyenera kumawerenga mau a Mulungu ndichakuti Mulungu safuna kuti inu mukaonongeke, koma kuti

muchokekuifa ndi kupita kumoyo. Inu, mukhoza kutembenukira kwa Mulungu ndi kulandira chipulumutso mwanjira yodabwitsa chomwe anakusungirani.

Wokondedwa anzanga apaulendo, kodi mumadziwa kuti simungaletse Mulungu kuti asakukondeni inu?Taonani!ndizotheka inu kukana chikondi chake, koma simungathe kumletsakukukondani ayi. Kutanthauza kuti inu mulibe mphamvu yoletsa mvula kugwa, koma mukhoza kutchigamvulayo ndi umbrella kuti isakugwereni.Mwanjira yomweyo tikunena kuti inu, mukhoza kukweza umbrella yotsutsana naye, ya tchimo lililonse kapena umbrella yomugalukira Mulungu ndi cholinga chakuti musalandire chikondi chake, koma sizikutanthauza kuti mukhoza kulepheretsa Mulungu kukukondani inu ayi. Nkhani ikunena kuti inu mukhoza kumunyoza Mulungu monga momwe mungathere, koma sizingatheke kuletsa Mulungu kuti akhumbekukupulumutsani, popeza adatuma Mwana wake yekha kuti afe m'malo mwa inu ndi ine. Tere, Ambuye Yesu ali wokonzeka kukupulumutsani ngati inu lero mungalandire chipulumutso chomwe akupereka kwa inuchi. Tikunena kuti inu

simuyenerakuganiza kuti moyo udzapitilira kukhala chomwechi, popeza dziko lidzatha ndipo kuti chiweruzo chikubwera ndithu.Inu ndi ine, tikukhala m'dziko lomwe likupitakuchiweruzo.Kodi inu mwakonzekera motani chiweruzochi?

10. Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyambaidzapita ndi chibumo chachikuru, ndi zam'mwambazidzakanganuka ndi kutentha kwakukuru, ndipo dziko ndi ntchito ziri momwemo zidzatenthedwa.

Pamene Mtumwi Petro akunena kuti, "Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala usiku," akugwirizana ndi Mtumwi Paulo pa 1 Atesalonika 5:2, pamene akuti, "Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku." Nkhani ikuti mau akuti "tsiku la Ambuye" amayimira nthawi yotalika yomwe idzayamba ndi chibvuto chachikulu, motsagana ndi zaka chikwi za ulamuliro wa Kristu pansi pano, kenaka satana adzalamulira kwa nthawi yochepa pamenepo chiweruzo chachikulu chotsiriza chidzafika. Ndipo monga tiwerenga m'buku la Chibvumbulutso, m'Mwamba ndi dziko latsopano zidzafika.

Mau akuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku, akutanthauza kuti pali chitsimikizo chonse kuti tsiku ili likudza ndithu mosakaika konse, koma lidzadzamodzidzimutsa monga momwe mbala imadza usiku kufuna kuononga chuma. Ndiye ngakhale pakali pano papita zaka zochuluka zoposa zikwi ziwiri, kuchokera pamene kalata iyi idalembedwa, ndipo tsiku limeneli lisanafike, koma likudza ndithu. Ichi, ndicho chiganizo chomwe Paulo pa Ahebri 9:27, akunena kuti, “Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa chiweruziro.” Kutsimikiza kuti inu muyenera kukhala wokonzeka kuti tsiku lina mudzaperekazanu zonse zomwe mwakhala mukuchita pansi pano.Koma chokhumudwitsa ndi chakuti tsiku limeneli lidzadzamodzidzimutsa monga mbala usiku, pamene inu ndi ine, tidzakhalatilikugona mopanda chiyembekezo china chilichonse cha tsiku la Ambuye. Tikunena kuti tsiku ili, lidzadza patsiku lomwe inu mukhoza kuliona kuti ndilosayenera komanso lokaikitsa, pamene mtima wanu wakhazikika ndipo pamene tsiku la Ambuye lidzadza. Pachifukwa chimenechi, tiyenera kusamala m’maganizo athu kuti sitiyenera kuika tsiku limeneli kutari, koma kuliika

pafupi ndiko.Kutanthauza kuti ife, wokhulupirira sitiyenera kuika kutari tsikuli monga mwaganizo la anthu osakhulupirira.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, tsiku la Ambuye ndilo loopsa kwambiri monga Malaki 4:5, akunena kuti, “Taonani, ndidzakutumizirani Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikuru ndi loopsa la Yehova.” Kutsimikiza kuti inu ndi ine, tiyenera kukhala anthu anzeru pakukonzekera tsiku limeneli kuti lisakhale tsiku la chionongeko kwa ife, ngati tingaike maso athu pazinthu za dziko lapansi.

Kwalerotilekeza pano. Koma timasanthula 2 Petro 3:5-10, momwe timakambirana za chikonzero cha Mulungu chapadziko lapansi. Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!